

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

KUFANANIZA MAPANGANO AWIRI

(Nkhaniyi yachokera pa Agalatiya 4:21-31).

Abrahamu, kholo la mu Chipangano Chakale, anali ndi ana aamuna awiri. Mulungu anamulonjeza Abrahamuyo pamodzi ndi mkazi wake Sara amene anali wosabereka kuti lye adzawadalitsa ndi mwana wammamuna mu ukalamba wao. Chifukwa chakusowa chikhulupiro, Sara anamupatsa Abrahamu mdzakazi wake, dzina lake Hagara, amene anamuberekera Ismaele. Mwana wammamuna uja amene analonjezedwa ndi Mulungu anabadwa kwa Sara pamene iye anali ndi zaka 90 ndipo Abrahamu ali ndi zaka 100. Ismaele anabadwa kudzera mu chiyanjano cha thupi ndi mdzakazi amene sanali mfulu pamene Isake anabadwa kwa mayi amene anali mfulu wolonjezedwa ndi Mulungu.

Iyi ndi nkhani yokoma imene ikufananiza Mapangano awiri amene Mulungu wakhala akuwagwiritsa ntchito polamulira anthu pa nthawi zosiyanasiyana – dongosolo la chilamulo ndi la Uthenga wabwino. Hagara ndi Ismaele anali monga Phiri la Sinai pamene Mulungu anakhazikitsa pangano loyamba ndipo anapereka chilamulo kwa Mose. Ana a Israele anali akapolo ku miyambo, zikhaldwe, ndi zolamulira za chilamulo. Mu Pangano loyambali,

dongosolo la chilamulo linali lochokera mu thupi monganso m'mene Ismaele anabadwa kuchokera mu thupi. Hagara sanali mfulu ndipo amabereka ana ake pansi pa malamulo a ukapolo.



Chimodzimodzinso, onse anabadwa pansi pa chilamulo la Mose anali mu goli ku dongosolo limene iwoakanatha kukwanitsa kutsatira malamulo ake kwathunhu.

Isake, wobadwa mwa chikhulupiro, mwana wa lonjezo kudzera mu kulowererapo kwa Mulungu, amayimira pangano latsopano limene Mulungu anapangana ndi anthu kudzera mwa mwana wake Yesu Khristu. Atakula Isake anaposa m'bale wake Ismaele. Isake anali kufanizira Khristu, yemwe anadziperekira yekha pa guwa la nsembe pomvera chifuniro cha Atate. Pangano la Mulungu ndi Abrahamu linakwanirtsidwa kudzera mwa Isake amene kuchokera mwa iye munatuluka mtundu wamphamuwa wa anthu amene ali osankhika a Mulungu.

Pali kusianitsa pakati pa Sinai ndi Yerusalemu. Yerusalemu, ngakhale anali pansi pa ukapolo wa chilamulo cha Mose komanso boma la ulamuliro wa Ufumu wa Aroma, anali malo amene kunali kachisi amene anthu amakapembedzerako Mulungu. Linali likulu la chikhulupiro chatsopano cha Chikhristu. Yerusalemu wauzimu, pomusianitsa ndi Sinai, akuyimira malo amene nzika zake zonse zimabadwira pansi pa pangano latsopano ndipo ali afulu.

“Koma Yerusalemu wa kumwamba uli waufulu, ndiwo amai wathu” (26). Akhristu enieni, okhala pansi pa pangano la uthenga

(Yapitirira pa tsamba 2)

ZIMENE BAIBULO

Limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akor. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhaliwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba !)

wabwino, ali omasulidwa ku ukapolo wa chilamulo pamodzi ndi miyambo komanso makhalidwe ake. Iwo ali afulu ku uchimo ndipo alibe kutsutsidwa. Iwo anabadwa osati kwa mdzakazi koma kwa mai amene anali mfulu.

Monga Hagara ndi mwana wake anatayidwa kunja, chomwechonso mtumwi Paulo analangiza mpingo kuti utayire kunja pangano lakale. "pakuti sadzalowa nyumba mwana wa mdzakazi pamodzi ndi mwana wa mfulu" (30). Isake anali mwana wa lonjezo, iye anali wochokera mu chikhulupiriro, ndipo cholinga cha Mulungu pa mtundu wa Ayuda chinakwaniritsidwa mwa iyeyu ndipo anali wolandira cholowa chonse cha atate ake. Chilamulo cha Mose chiyenera kutayidwa kuti m'malo mwake tilandire pangano latsopano. Akhristu, amene ali otsatira a Yesu Khristu, ali ana a lonjezo.

as Anthu ena amakakamira lemba la chilamulo cha Mose kapena kumaganizira kwambiri za pangano lakale lija ngakhale kuti panopa iwo akukhala pansi pa Uthenga Wabwino Izzi zimapangitsa kuti munthu akhale mu ukapolo. Tayirani kunja pangano lakalelo ndipo musangalale ndi ufulu komanso kumasuka zimene zili pansi pa pangano la Uthenga Wabwino, popeza "abale, sitili ana a mdzakazi, komatu a mfulu" (31).

—mws

**Onani webusayiti yathu yatsopano!
Mupezamo makalata onse a m'mbuyomu.**

www.thegospeltruth.org

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choondi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & René Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choondi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu illyonse molingana ndi chitsogozzo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choondi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zafulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, 605 Bishops Ct., Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Koma tsopano lye [Khristu] walandira chitumikiro chomveka koposa, umonso ali Nkhoswe ya pangano labwino loposa, limene likhazikika pa malonjezano oposa.

—Ahebri 8:6

Ndi chinthu chamwayi kwambiri kukhala mu nyengo ino ya chisomo ndi choonadi. Yesu Khristu amene ali Nkhoswe ya pangano latsopano, anakhazikitsa pangano labwino koposa ndi anthu. Panganolo lili ndi malonjezano abwino. Pangano lakale linali ndi malonjezo a zinthu zabwino zathupi ndi zapadziko komanso chiteteko cha dziko. Pangano latsopano limalonjeza madalitso auzimu ndi amuyaya.

Mtolo umene ndikufuna ndigawane nanu ulendo uno ndi wa mapangano awiri amene Mulungu anapangana ndi anthu. Umenewu ndi mutu wofunikira kwambiri chifukwa umayala maziko a pamene tikhazikikepo mtsogolo muno pamene tidzakhale tikukamba za mitu monga Kusiyana kwa chakhumi ndi chopereka, Kusunga Sabata, Kusiyana kwa kupembedza kwathupi ndi kupembedza kwauzimu.

Nthawi zambiri anthu amadabwa ngati pali kufunikira kulikonde kwa Chipangano Chakale makamaka popeza tikukhala m'nthawi ya Chipangano Chatsopano. Yankho lake mosapeneka konse ndi INDE! Chipangano Chakale ndi nkhanzi ya Mulungu ndiponso ubale wake ndi munthu. Mu Chipangano Chakale timaphunziramo za chikhaliidwe cha Mulungu cha chiyero komanso chikhaliidwe cha uchimo cha munthu. Baibulo ndi buku limene lili lodzaza ndi maphunziro ozama auzimu, chilimbikitso, mbiri, komanso mauneneri a Mesiya amene akubwera. Atumwi aja ngakhalenso Khristu mwini ananenapo za mau ena ndi ena kuchokera mu Chipangano Chakale.

Pangano lakale linapita ndipo panopa sititsatiranso Lamulo la Mose ndipo sindife akapolo ku lamuloli. Tikudziwa kuti zonna zambiri zimene zimapezeka m'menemo monga malamulo ochokera kwa Mulungu sizinasinthe ndipo zinalimbikitsidwa mu Chipangano Chatsopano. Pamene Malemba a mu Chipangano Chakale ali othandiza kuti timvetsetse bwino, sitienera kutenga Chipangano Chakale pachokha ndi kuchigwiritsa ntchito ngati maziko pamene tikufuna kumanga chiphunzitsio ichi m'masiku athu a chisomowa. Anthu ena amangotola ndi kusankhapo zimene akufuna kuti adzichita kuchokera ku Chipangano Chakale. Iwo amasunga Sabata ndi kugwiritsa ntchito zida zoyimbira, koma safukiza lubani popemphera kapena kupereka nsembe. Nkoyenera kuti anthu amvetsetse kwathunthu pangano lakale limene linasinthidwa, ndipo mmalo mwake pali lina, lomwe lili pangano loposa.

Ambiri mwa makolo athu a m'Chipangano Chakale anawonetsa zitsanzo za kulimba mtima, chikhulupiro ndi kudzipereka. Tiyeneranso kukumbukira kuti iwo anali pansi pa chilamulo ndipo analibe chisomo cha Mzimu Woyeria m'mitima mwawo. Chifukwa cha ichi nkulakwa lerolo kutsatira ndi kutengerapo chitsanzo pa china chilichonse chimene anachita popembedza ndi m'makhalidwe awo.

Ntchito za chilungamo zoonekera kunja sizilungamitsa mtima. Kusangalala chifukwa chakuti tamasulidwa ku lamulo sikutanthaiza kukhala m'moyo wolekerera, komatu zonna zake nzakuti kukhala pansi pa chisomo kumatifikitsa chifupi mu ubale wathu ndi Mulungu. Muyeso wa chiyero tsopano umayamba ndi munthu wamkati.

Michael W. Smith

October 2016

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira


makalata athu kapenango

kuti muone. makalata

akale.

KALOZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

Mutu: Mapangano Awiri



Kuwerenga Malemba: Pakuti ili ndi pangano ndidzalipangana ndi nyumba ya Israele atapita masiku ajawa, anena Ambuye: Ndizapatsa malamulo anga kuwalonga m'hzeru zao, ndipo pamtima pao ndidzawalemba iwo; ndipo ndidzawakhalira iwo Mulungu, ndipo iwo adzandikhalira Ine anthu —Ahebri 8:10

Mwachidule: Pangano lakale, limene Mulungu anakhazikitsa kudzera mu Lamulo loperekedwa kwa Mose, silinali langwiro kuti likwanitse kubweretsa chilungamo chenicheni kwa anthu. Pangano latsopano linakhazikitsidwa kudzera mu kudzipereka nsembe komanso Unsembe wa Yesu Khristu limene linabweretsa ufulu ndi chiyero chenicheni.

Chidziwitso: Ngakhale mitu ya nkhanu yaperekedwa, malemba othandizira kuti timvetse bwino ayikidwa pansi pa mitu yosiyanasayana .

I. Pangano Lakale Likhazikitsidwa

- A. Eksodo 34:28 Mau a panganolo, Malamulo Khumi.
- B. Deuteronomo 5:1-3 Kupanga Pangano ndi Israele.
- C. Malaki 4:4 Lamulo la Mose = Pangano lakale.

II. Cholinda cha Lamulo

- A. Agalatiya 3:24-25 Lamulo linali namkungwi.
- B. Aroma 7:7-8 "Popanda Lamulo, uchimo unali wakufa."
- C. Aroma 3:19-20 Lamulo limatidziwitsa za uchimo.

III. Kufananiza Mapangano Awiri

Agalatiya 4:21-31 Hagara ndi Sara; Ismaele ndi Isake; Phiri la Sinai ndi Yerusalem; ntchito ndi chikhulupiriro; ukapolo ndi ufulu.

IV. Pangano Loposa ndiponso latsopano Likhazikitsidwa

- A. Yeremiya 31:31-33 Pangano latsopano likuloseredwa.
- B. Ahebri 8:6-12 "Ndizapangana nawo pangano latsopano."
- C. Yohane 1:17 Chisomo ndi choonadi zinadza ndi Yesu Khristu.
- D. Aefeso 2:13-16 Kuyanitsidwano ndi Mulungu kudzera mwa Khristu.
- E. Mateyu 26:27-28 Mwazi wa Khristu mu Chipangano Chatsopano.
- F. Agalatiya 3:13-14 Kuomboledwa ku temberero la lamulo.
- G. Yohane 8:31-36 Choonadi chimamasula.

V. Yesu—Mkhalapakati Mmodzi/Nsembe Imodzi/Wansembe Mmodzi

- A. Ahebri 9:11-16 Khristu ndi nsembe yoposa komanso wansembe woposa.
- B. Ahebri 10:11-18 Yesu anapereka nsembe yamachimo kamodzi kokha koma kwamuyaya.
- C. Aroma 6:10 Yesu ndi nsembe yomaliza ya uchimo.
- D. Ahebri 7:20-22 Unsembe wa Khristu.
- E. I Timoteo 2:5 Yesu ndi yekhayo anali mkhalapakati wa

Mulungu ndi anthu.

VI. Kuperewera kwa Lamulo

- A. Ahebri 10:1-4 Lamulo linali chithunzithunzi cha zinthu zabwino zimene zilinkudza.
- B. Aroma 8:3-4 Lamulo linali lopanda mphamvu (Ahebri 8:7; 10:11).
- C. Ahebri 7:11-12 Unsembe wa Alevi komanso Lamulo zinasinthidwa.
- D. Ahebri 7:17-19 Kusandutsa Malamulo kuti akhale opanda ntchito.

VII. Pangano lakale linachotsedwa

- A. Ahebri 10:9-10 Pangano loyamba linachotsedwa.
- B. Ahebri 8:13 Pangano Lakale linasinthidwa ndi Pangano Latsopano.
- C. Aroma 6:14 Inu simulinsa pansi pa Lamulo.
- D. Aroma 7:6 Munamasulidwa kuchokera ku Lamulo.

VIII. Kukwanirtsidwa kwa Lamulo

- A. Mateyu 5:17 Yesu anabwera kudzakanirtsia Lamulo.
- B. Aroma 13:8-10 Chikondi ndiko kukwanirtsia Lamulo.

IX. Kukhala m'moyo wapamwamba ndi Pangano latsopano

- A. Mateyu 5:31-48 "Kunalembedwa kuti...koma ine ndinena ndi inu."

X. Chilungamo Chenicheni kudzera mwa Chikhulupiriro

- A. Agalatiya 2:16 Kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro mwa Yesu Khristu.
- B. Aroma 9:30-32 Chilungamo nchochokera ku chikhulupiriro osati mwa ntchito za Lamulo.
- C. Agalatiya 5:2-4 Khristu ali wosapindulitsa kudzera mu kusunga Lamulo.

Kumaliza: Koma podziwa kuti munthu sayesedwa wolungama pa ntchito ya lamulo, koma mwa chikhulupiriro cha Yesu Khristu.... —Agalatiya 2:16

Mapangano Awiri

CHIKONZERO CHA KUMWAMBA

Kuyambira pa nthawi ya kulengedwa kwa dziko, Mulungu anali ndi chikonzero chake pa mtundu wa anthu. Pamene Adamu ndi Hava anachimwa m'munda mwa Edeni, Mulungu anali akugwirabe ntchito kuti abwezeretse mtundu wa anthu ku malo a chipulumutso champhumphu. Kukwanirtsidwa kwake kwa zimene Mulungu ankafuna kuchita sikuti kunali kooneratu nthawi yomwego, koma pamene zaka zochuluka zinali kudutsa, kukongola ndi mphamvu za chikonzero chenicheni cha chipulumutso zinavumbulutsidwa kudzera mu kubwera kwa Yesu Khristu.

MAPANGANO A MULUNGU

Baibulo ndi buku la ulendo wa munthu komanso ubale wake ndi Mulungu. Kupyolera mu nthawi zosiyaniyana, Mulungu wakhala akufuna zinthu zosiyaniyana kuchokera ku mibabdwo yosiyaniyana. Nkofunikira kumvetsetsa ndondomeko komanso mfundu zimene Mulungu amagwirira ntchito ndi anthu masiku ano. Mfundu zokhazikika zimene Mulungu amagwirira ntchito ndi anthu zimatchedwa M'malemba kuti Mapangano." Mapangano a M'malemba kuchokera kwa Mulungu anali oposa mgwirizano wa Mulungu ndi munthu. Pangano limawulula momveka bwino za malonjezo ndi malangizo a Mulungu popeza kudzera mwa iwo lye anapereka kwa munthu kukonderedwa kwake ndi madalitso ake.

PANGANO LOYAMBA

Loyamba mwa mapangano awiri linapatsidwa kwa Mose pa Phiri la Sinai. "Ndipo Yehova anati kwa Mose,... ndapangana ndi iwe ndi Israele....Ndipo analembera pa magomewo mau a panganolo, mau khumiwo" (Eksodo 34:27-28). Pangano limeneli munali malamulo ndi mawerozo onse amene anaperekedwa kwa Mose (Deuteronomo 5:1-3). Pangano limeneli, limene limatchedwanso kuti "Lamulo la Mose" (Malaki 4:4), linapangidwira makamaka Ayuda ndipo Lamulolo kapena cholowa chake sizinaperekedwe kwa anthu onse (Aroma 2:14). Lamulo la Mose linali ndi malamulo owongolera okhudzana ndi milandu ya pa chiweniweni, makhaldwe a umunthu komanso

miyambo yosiyaniyana. Ayuda anawuzidwa m'mene angapembedzere Mulungu komanso analangizidwa kuti adziperekwa nsembe zosiyaniyana chifukwa cha machimo awo ndi mphulupulu zavo. Pangano ili linaperekedwa pokonzekera pangano lina lachiwiri komanso lomaliza limene linaperekedwa kudzera mwa Yesu Khristu. Lamulo linali ngati "mthonzi wa zokoma zilinkudza" (Ahebri 10:1-4), pakuti sikutheka kuti mwazi wa ng'ombe zamphongo, ndi mbuzi uchotse machimo. Choncho munthu akachimwa, chopepesera machimo chinali kuchitika kwa kanthawi kochepa. Anthu amapembedza Mulungu mwachithupithipi komanso mongokwanirtsitsa mwambo, koma mitima yayo sinali yoyeretsedwa ndi ntchito za chilamulo kapenango nsembe zimene iwo amaperekira. Lamulo linali lofooka kudzera m'thupi (Aroma 8:3) and silinathe kupanga chilichonse kuti chikhale changwi (Ahebri 7:19).

NAMKUNGWI

Ngakhale linali losakwanira, pangano loyambalo linaperekedwa kwa anthu pa chifukwa—kuwakonzekeretsa anthu kulandira nsembe yangwi imene ili Yesu Khristu amene anatiyanjanitsa anthufe ndi Mulungu. "Momwemo chilamulo chidakhala namkungwi wathu wakutifikitsa kwa Khristu, kuti tikayesedwe olungama ndi chikhulupiro. Koma popeza chadza chikhulupiro, sitikalanso omvera namkungwi" (Agalatiya 3:24-25). Lamulo linatidziwitsa za uchimo (Aroma 3:19-20). "Pakuti popanda lamulo uchimo uli wakufa" (Aroma 7:7-8). Lamulo la Mose ndi limene linavumbulutsa kuchimwa kwa munthu, kufooka kwake komanso kulephera kwake kuti agonjetse uchimo kudzera mu ntchito ndi machitachita a thupi.

PANGANO LACHIWIRI

Kuyambira kale, Mulungu anakonzeratu kuti adzapange pangano labwino ndi anthu. "Taonani masiku adza, ati Yehova, ndipo ndidzapangana pangano latsopano ndi nyumba ya Israele, ndi nyumba ya Yuda...Koma ili ndi pangano limene ndidzapangana ndi nyumba ya Israele atapita masiku aja, ati Yehova; ndidzaika chilamulo changa m'kati mwao, ndipo m'mtima mwao

(Yapitirira pa tsamba 6)




"Pakuti sikutheka kuti mwazi wa ng'ombe zamphongo, ndi mbuzi ukachotsera machimo."

ndidzachilemba; ndipo ndidzakhala Mulungu wao, nadzakhala iwo anthu anga” (Yeremiya 31:31-33). Pangano latsopanoli silimadaliranso malamulo olembedwa pa magome a miyala. Pa Yohane 1:17 akunena kuti “chilamulo chinapatsidwa mwa Mose; chisomo ndi choonadi zinadza mwa Yesu Khristu.” Ngati pangano loyambali linalibe chifukwa, sipakadakhalanso chifukwa chofunira pangano lachiwiri (Ahebri 8:6-12).

KUPAMBANA KWA PANGANO LATSOPOANOLI

Pangano latsopanoli ndi loposa lakale lija, popeza munthu anayanjanitsidwa ndi Mulungu kudzera mu imfa ya Khristu pamtanda. Iye anathetsa Lamulo ndi zolamulira zake (Aefeso 2:13 -16). Anatayira kunja lamulo la pangano lakale, nsembe za nyama, ndi kupembedza kotsatira miyambo. Pangano latsopanoli silitsamira pa ntchito koma kukhala ndi chidziwitso cha

“Chifukwa chake ngati Mwana adzakuyesani inu aufulu, mudzakhala mfulu ndithu.”



chikhulupiro mwa Yesu. Iye “anatiombola ku temberero la chilamulo” (Agalatiya 3:12-14). Imfa komanso chilango cha Lamulo zinakhala zopanda ntchito ndipo njira ya chikhululukiro ndi moyo zinaperekedwa. Yesu anakhetsa mwazi wake “wa pangano wothiridwa chifukwa cha anthu ambiri ku kuchotsa machimo” (Mateyu 26:27-28). Nsembe yake yangwiyo inachita zimene mwazi wa ng’ombe zamphongo ndi mbuzi sukanachita. Mwazi wake unayeretsa chikumbumtima kuchokera ku ntchito zakufa kuti titumikire Mulungu wamoyo (Ahebri 9:11-16). “Pakuti ndi chipereko chimodzi anawayesera angwiyo chikhaliire iwo oyeretsedwa....Koma pomwe pali chikhululukiro cha machimo palibenzo choperekha cha kwa uchimo” (Ahebri 10:11-18). Pangano latsopanolo, limene lili la mwazi wake linatibweretsera ufulu kuchokera ku mphamu yeniyenyo ya uchimo. “Indetu, indetu, ndinena kwa inu kuti yense wakuchita tchimo ali kapolo wa chimolo....Chifukwa chake ngati Mwana adzakuyesani inu aufulu, mudzakhala mfulu ndithu (Yohane 8:31-37).

Ungwiyo sumabwera kudzera mwa Unsembe wa Alevi kapena kudzera mwa chilamulo. Tsopano Yesu Khristu ndiye Mkulu wa ansembe wamkulu (Ahebri 4:14) wa pangano loposa (Ahebri 7:20

-23). Monga panali kusintha pa dongosolo la Unsembe, chomwechonso panayenera kuti pakhalenso kusintha pa Lamulo (Ahebri 7:11-13). “Pakuti chimene chilamulo sichinathe kuchita, popeza chinafooka mwa thupi, Mulungu anatumiza Mwana wake wa lye yekha m’chifanizo cha thupi la uchimo, ndi chifukwa cha uchimo, natsutsa uchimo m’thupi; kuti choikika chake cha chilamulo chikakwaniridwe mwa ife, amene sitiwendayenda monga mwa thupi, koma monga mwa mzimu” (Aroma 8:3-4).

PANGANO LAKALE LINATHETSEDWA

Chifukwa cha kubwera kwa pangano la chisomo, pangano lakale lija linasiyidwa. “Pakunena lye, Latsopano, anagugitsa loyambali. Koma chimene chilinkuguga ndi kusukuluka, chayandikira kukanganuka.” (Ahebri 8:13). Pa Ahebri 10:9 akunena kuti “Achotsa choyambacho, kuti akaike chachiwiricho.” Pakuti uchimo sudzachitanso ufumu pa anthu; “popeza simuli a lamulo koma a chisomo” (Aroma 6:14).

MUYESO WAPAMWAMBA PANXI PA CHISOMO

Yesu sanabwere kudzaononga chilamulo koma kudzakwaniritsa (Mateyu 5:17). Ngakhale anthu sali pansi pa chilamulo cha Mose, pali mfundo zambiri zimene zinabwerezedwa mu Pangano latsopano. Pansi pa chisomo, chilamulo chinalembewa m’mitimwa mwathu ndipo tili ndi mphamu zokhala monga mwa chilamulocho. Aroma 13:8-10 imalongosola momveka bwino m’mene chikondi choona cha Mulungu chimakwaniritsira chilamulocho. Pansi pa chisomo, anthu ambiri amasangalala ndi ufulu wao, ndipo akuyeneradi kutero, komabe ubale wathu ndi Mulungu mwachisomo umatipangitsa kuti tikhale m’moyo wachiyero chenicheni. Pali muyeso wa moyo wapamwamba pamene tikhala pansi pa pangano latsopano monga Khristu anationetsera pamene anawonetsa kusiyana kwa chilamulo ndi zofunikira za kukhala m’moyo wa chisomo pa Mateyu 5.

TALANDIRA CHIPULUMUTSO

Pansi pa chilamulo cha Mose, anthu samapeza chilungamo chenicheni ndipo palibe munthu amene amayesedwa wolungama chifukwa cha ntchito zabwino za chilamulo. Munthu amayesedwa wolungama chifukwa cha chikhulupiro chake mwa Yesu Khristu yekha (Agalatiya 2:16). Chipulumutso ndi cha chisomo kudzera mwa chikhulupiro ndipo onse amene akufunabé kulungamitsidwa kudzera mu ntchito pansi pa pangano lakale kapena latsopano amamupangitsa Khristu kukhala wopanda mphamu ndipo atayika kuchokera ku chisomo (Agalatiya 5:2-4).

Pangano lakale la kwa Ayuda linapita ndipo pano pali pangano latsopano ndi loposa limene lili kwa anthu onse. Pansi pa pangano latsopanoli kudzera mu mwazi wa Yesu, anthu amapeza chikhululukiro kuchokera ku machimo komanso mphamu zokhalira m’moyo wachiyero ndi waumulungu. Chipangano Chakale ndi chofunikirabe popeza chimatiphunzitsa zambiri za Mulungu ndi uchimo, komabe panganolo palokha ndi lopanda pake. Tiyamika Mulungu chifukwa cha chisomo ndi ufulu zimene zili mwa Khristu Yesu.

Pangano Lakale

Pangano Latsopano

1. La Aisraele
2. Linaleembedwa pa Magome a Miyala
3. Pangano la Kalata
4. Unsembe wa Alevi
5. Chihema chapansipano
6. Lamulo la Ntchito
7. Lamulo la Uchimo ndi la Thupi
8. Limabweretsa Ukapolo ndi Imfa
9. Nyama Zambiri zimaperekedwa
nsembe chifukwa cha Uchimo
Nsembe yopepesera machimo cha-
10. ka chilichonse / Palibe Chipulumutso
11. Kupereka Chakhumi
12. Kutsata Sabata
13. Kupembedza Kwathupi
(Zofukiza, zida za mayimbidwe)
14. Ndi Chithunzithunzi chabe
15. Linathetsedwa

1. La Anthu Onse
2. Lolembedwa M'mitima ya Anthu
3. Pangano la Mzimu
4. Mkuluwansembe Mmodzi —Yesu
Khristu
5. Chihema Chauzimu
6. Kulungamitsidwa mwa Chisomo ndi
Chikhulupiro
7. Lamulo la Chiyero ndi la Mzimu
8. Limabweretsa Ufulu ndi Moyo
9. Nsembe imodzi yokwanira —Yesu
Khristu
10. Nsembe yopepesera machimo ya-
muyaya / Chipulumutso chamuyaya
11. Chopereka Chafulu
12. Kukhala Woyerwa kwa Ambuye Tsiku
Lililonse
13. Kupembedza kwa uzimu kuchokera mu
Mtimu
14. Zoona zenizeni
15. La Muyaya

*Pakuti loyamba lija likadakhala lopanda
chilema sakadafuna malo a lachiwirilo.*


Ahebri 8:7



KODI MUKUDZWA?

Malamulovo athetsedwa, choonadi cha asanu ndi anai mwa Malamulo Khumi chinabwezeredwanso pansi pa chisomo chopezeka mu Chipangano Chatsopano.

Lamulo lachinai, “Udzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika” (Eksodo 20:8), ndi lokhalo limene sitienera kulibwereza. Mfundu imeneyo inali chithunzithunzi chabe cha nthawi imene ikubwera mu Chipangano Chatsopano pamene tsiku LILILONSE limayenera kusungidwa ndi kukhala lopatulika ndi loyera kwa Ambuye.



Chifukwa chake Chilimikani mu Ufulu

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA
Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Khristu anatisandutsa mfulu, kuti tikhale mfulu; chifukwa chake chilimikani, musakodwenso ndi goli la ukapolo. —Agalatiya 5:1

Paulo amawadandaulira Akhristu kuti achirimike mu ufulu komanso kumasuka kumene anali nako mwa Khristu Yesu. Iye samawalimbikitsa kuti akhale m'moyo wachisawawa ndi wauchimo koma amawachenjeza kuti asakodwe mu goli ndi ukapolo wa Lamulo.

Akhristu ambiri masiku ano ali mu ukapolo ku “lamulo la uzimu” pamene akunena kuti akumana ndi chisomo mwa chikhulupiriro. Iwo amatenga zinthu za uzimu potsata lamulo ndipo zinthu zofunikira monga ubale wa chikondi ndiponso chikhulupiriro zimabisika mu malamulo akuti “chitani izi ndipo izo musachite.” Iwo sanadziwebe kuti chilemba chimapha koma Mzimu amapereka moyo. Mzimu Woyera amafunitsitsa kuwombola oyera mtima oterewa a mu Chipangano Chatsopano.



Atumiki a choonadi, sangalalani ndi ufulu wanu ndipo musaope kukondwera chifukwa cha chisomo ichi mu nyengo ino ya uthenga wabwino. Ufulu umenewu supezeka pokhala kapolo wa Lamulo kapena potsata zolamulira za oyera mtima zimene zimanenedwa ndi zosanenedwa zomwe. Ufulu ndi kumasuka zimapezeka mu kutumikira Ambuye mwa chiyero chifukwa cha chilungamo cha Mulungu chimene chili mkati mwathu. Mtima umafuna kukondweretsa Mulungu modzipereka kwathunthu komanso mwachikondi. “Woyera mtima wotsata lamulo” ndi woyera mtima wotsata chisomo” onse akhoza kufika pa mfundo yofanana pa m'mene tingakhalire m'moyo, komabe mmodzi ali mu ukapolo pamene winayo mwachimwemwe amapeza kumasuka chifukwa cha ntchito ya chisomo ya Mulungu yochitika m'moyo wake tsiku ndi tsiku.

—mws